

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

Malangizo ndi Chilimbikitsa kuchokera m'Baibulo kupita kwa amene akulalikira Uthenga Wabwino

KUKHALA MDINDO PACHUMA

Baibulo limakamba nkhani ya ndalama, chuma ndi zonse zokhudza katundu wa munthu koposa mutu wina uliwonse wopezeka m'malemba. Pali mavesi oposa 2,000 pa mutu umenewu popeza umakhudzana ndi moyo wathu wa zachuma komanso wauzimu.

Kagwiritsidwe ntchito ka ndalama komanso katundu wathu ndi gawo lofunikira kwambiri pa moyo wathu wa tsiku ndi tsiku ndiponso zimathandizira pakukwaniritsa ntchito imene Mulungu anatipatsa yosamalira banja, kuthandiza osauka ngakhalenso kufalitsa uthenga wabwino. Chifukwa chakuti ndalama zimagwira ntchito yofunikira pa moyo wathu, Mulungu mwa nzeru zake zopanda malire, anatipatsa chiphunzitso cholongosolera za nkhanayi kuti mkhristu atsatiye pambali popereka mfundo zabwino zachuma zakuti tikhoza kuzigwiritsa ntchito. M'mene chilili chuma cha munthu zimathandizira kaganizidwe komanso momwe amachitira zinthu, zimene pamapeto ake zimathandizira pa moyo wake wauzimu. Chifukwa cha ichi, nkofunikira kuti tsiku ndi tsiku pamene Akhristu akuyenda ndi Mulungu, adzikhala ndi kaganizidwe koyenera ka zinthu zokhudza ndalama molingana ndi m'mene Baibulo likunenera.

Ngakhale kuti dziko lapansi lili ndi kaganizidwe kolakwika kokhudzana ndi umwini wa zinthu kamene kamabwera chifukwa cha mtima wa umbombo, nsanje ndi dyera, Baibulo limaonera mosiyana kwambiri pa mfundo yokhudza katundu wa munthu. "Pachiyambi Mulungu adalenga kumwamba ndi dziko lapansi" (Genesis 1:1). Zinthu zonse ndi za Mulungu ndipo "Mphatso iliyonse yabwino... zichokera Kumwamba" (Yakobo 1:17).

Mulungu wapereka kwa anthu ntchito yakuti pokhala adindo ake, asamalire bwino

chilengedwe chake chonse. Dzikoli likanasintha kukadakhala kuti anthu anamvetsetsa kuti zinthu zonse ndi za Mulungu osati zathu. Ifeyo ndife adindo chabe a zinthu zonse zimene tili nazo ndipo zisankho zathu zidzichitika poganizira kuti tikulemekeza Mulungu. Ndi "chikondi cha ndalama" (1 Timoteo 6:10) chimene chili "muzu wa zoipa zonse" osati ndalamayo ayi. Yesu ananena kuti "Palibe munthu angathe kukhala kapolo wa ambuye awiri...Simungathe kukhala kapolo wa Mulungu ndi wa Chuma." (Mateyu 6:24). Chifukwa cha ichi, Akhristu akuyenera kusamalitsa kuti asatumikire ndalama, koma kulola kuti ndalamazo ziwatumikire kwinaku akuzindikira kuti chuma chenicheni sichipezeka mu zinthu za padziko lino lapansi.

Mdindo wanzeru amapanga zisankho zimene sizili za undekha koma zimene zili zokondweretsa mbuye wake. Ifeyo pokhala adindo a Mulungu, tikuyenera kuti ndalama zathu tizilamulire ndi kuziyang'anira ndi chisamaliro komanso kukhulupirika komweko monga m'mene timachitira ndi zinthu zauzimu. "Komatu pano pafunika za adindo, kuti munthu akhale wokhulupirika" (1 Akorinto 4:2).

Yesu mwini anafunsa funso lofunikira kwambiri pa Luka 16:11, "Chifukwa chake ngati simunakhala okhulupirika m'chuma cha chosalungama, adzakhulupirira inu ndani ndi chuma choona?" Monga m'mene zilili mu fanizo la matalente (Mateyu 25:14-30), Akhristu akuyenera kukhala adindo okhulupirika a chuma ndi zinthu zonse zimene Mulungu wawapatsa. Kukhala mdindo pachuma kumatanthauza kulongosola bwino chuma mu njira yakuti Mulungu akondwera nayo kuyambira m'mene mwapezera ndalama, m'mene mukuzigwiritsira ntchito pa zofunikira zanu, m'mene mukuzisungira kuti zichuluke komanso m'mene mukuzisamalirira. ■



"Pokhala adindo a Mulungu, tikuyenera kuti ndalama zathu tizilamulire ndi kuziyang'anira ndi chisamaliro komanso kukhulupirika komweko monga m'mene timachitira ndi zinthu zauzimu."

Chiphunzitso cha Kusauka Ndi Chiphunzitso cha Kulemera

2

Mau a Mkonzi Mphamvu Imene Ipezeka Pokundika Chuma Mosalekeza

3

Kusanthula Baibulo: Kukhala mdindo pachuma

4

Mfundo za Baibulo Zokhudza Kukhala Mdindo Pachuma 5 Banja ndi ndalama

7

Kodi Mukudziwa?

Mau a Nyengo Yake

8

ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA ZA...

Mau a Mulungu

2 Tim. 3:16-17; 2 Pet. 1:20-21; Mat. 24:35

Ubale wa Chikondi

Mat. 22:37-40; Yoh. 14:21-23; 1 Yoh. 4:7-11

Kulapa

Mach. 3:19; Mach. 17:30; 2 Akor. 7:10

Kubadwa mwatsopano

Yoh. 3:3-7; 2 Akor. 5:17; Aro. 6:1-4;
Aef. 2:1, 5-6

Kupulumuka ku uchimo

1 Yoh. 5:18; Mat. 1:21; Yoh. 8:11

Chidzalo cha Mzimu Woyera

Mach. 19:2; Mach. 15:8-9; Mach. 1:8

Chihero

Luk. 1:73-75; Aheb. 12:14; 1 Pet. 1:15-16;
Tit. 2:11-12; Aro. 6:22

Ufumu wa Mulungu

Luk. 17:20-21; Aro. 14:17; Yoh. 18:36

Mpingo

Mach. 2:47; Aef. 4:4-6; 1 Akor. 12:12-13;
Akol. 1:18

Umodzi

Yoh. 17:20-23; Agal. 3:28; Chiv. 18:2-4

Maskaramenti

Mat. 28:19-20; Mat. 26:26-30;
1 Akor. 11:23-27; Yoh. 13:14-17

Machiritso

Luk. 4:18; Yes. 53:4-5; Yak. 5:13-16

Chihero cha Banja

Mat. 19:5-6; Luk. 16:18; Aro. 7:2-3;
1 Akor. 7:10-11

Chikhalidwe cha pakati pa anthu ena

1 Tim. 2:9-10; 1 Akor. 11:14-15; Deut. 22:5

Masiku omaliza

2 Pet. 3:7-12; Yoh. 5:28-29; 2 Akor. 5:10;
Mat. 25:31-46

Kukhala mwa mtendere

Luk. 6:27-29; Luk. 18:20

Kupembedza

Yoh. 4:23-24; Aef. 5:19; 2 Akor. 3:17

Kulalikira Uthenga Wabwino

Mrk. 16:15

CHIPHUNZITSO CHA KUSAUKA NDI CHIPHUNZITSO CHA KULEMERA

Chiphunzitso cha kusauka ndiponso chiphunzitso cha kulemera ndi ziphunzitso ziwiri zokhudza chuma zimene zili zosiyana ndipo zakhala zikulimbikitsidwa mu chipembedzo. Ziphunzitso ziwiri zosiyana zili ndi mavesi ake amene amazilimbikitsa koma zimatengedwera pamgong'o ndipo ndime zake sizigwirizana ndi zonena za mau a Mulungu. Chiphunzitso cha kusauka chimanena kuti chuma ndi choipa ndipo kukhala wosauka kumakondweretsa Mulungu. Chimaphatikizanso mfundo yakuti kukhala osauka mwadala ndi chinthu chopambana kwambiri. Chiphunzitso chimenechi ndi chomwe chinabweretsa moyo wa munthu wokhala payekha komanso amene amatenga lumbiro la kusauka. Chiphunzitso chimenechi chimakhazikika pa malemba akuti: "Odala ali osauka" (Luka 6:20, 24) ndiponso "Gulitsani zinthu muli nazo" (Luka 12:33). Kukhala ndi katundu kumatengedwa ngati temberero ndipo ntchito ya Mulungu ndiyo kupereka basi, ifeyo sitichitapo kanthu. Ngakhale zili choncho, anthu amene amatsatira chiphunzitso chimenechi nthawi zambiri amakhala akuyesetsa kukumana ndi zosowa zawo za tsiku ndi tsiku ndipo sakwanitsa kuthandiza osauka popeza iwowo nawonso amakhala osauka.

Chiphunzitso cha kulemera (uthenga wa kuchita bwino ndi kukhala ndi chuma) chimanena kuti madalitso a chuma pa ife ndicho cholinga cha Mulungu. Chiphunzitso chimenechi chimatsindika mfundo yakuti munthu ali ndi mphamvu yochitira zinthu ndipo Mulungu amamugwiritsa ntchito munthuyo pofuna kuti zinthu zichitike—ngati Akhristu ali ndi chikhulupiriro ndipo amamvera Mau a Mulungu, Mulunguyo adzawalemeretsa pamoyo wao wauzimu ngakhalenso wathupi. Chiphunzitso chimenechi chimakhazikika pa Malemba monga awa akuti: "Mukakhala nacho chikhulupiriro monga kambeu kampiru...palibe kanthu kadzakukanikani." (Mateyu 17:20) komanso "Ndipo zinthu zilizonse mukazifunsa m'kupemphera ndi kukhulupirira, mudzazilandira" (Mateyu 21:22). Chiphunzitso chimenechi chimakhazikika kwambiri pa mfundo yakuti munthu akhale ndi chikhulupiriro kuti alandire madalitso a Mulungu ndipo chimadziwika ndi mau akuti, "Mukachitchula, chimenecho chikhala chanu." Munthu wina wolembe ananena kuti chiphunzitso chimenechi chili ngati "Ufiti wa Chikhristu." Chimalemekeza zinthu za dziko lino ndipo molakwitsa chimafananiza kuti kukhala ndi chuma kumaonetsa kuti amenewo ndiwo madalitso ochokera kwa Mulungu.

Chiphunzitso cha umphawi ndiponso cha kulemera zonse zimaperewerabe pena. Palibe chenicheni chauzimu pakati pa chuma ndiponso pa umphawi. Kuvutika si chizindikiro chakuti munthuwe ndiwe wosamvera kapena kulemera kuti ndi chizindikiro chakuti Mulungu akuvomereza zimene ukuchita. Akhristu asamapembedze zinthu zimene ali nazo ndipo akuyenera kudzipereka ku kukhala wopereka moolowa manja. Iwo akuyenera kukhala ndi chikhulupiriro komanso kudalira Mulungu pa zinthu zonse. Iwo akuyenera kutsatira ubale wao ndi Mulungu mwini chifukwa cha kufunikira kwa ubalewo osati popeza akufuna madalitso a moyo uno. Pokhala adindo, Akhristu akuyenera kukwaniritsa mfundo zonse zopezeka m'Baibulo, osati zowerengeka chabe zimene zimalimbikitsa chiphunzitso cha munthu, kaya ndi cha umphawi kapena cha kulemera. ■

Gospel Truth ndi kalata imene imasindikizidwa miyezi itatu iliyonse ndi a mpingo wa Church of God pofuna kulangiza ndi kulimbikitsa kuchokera mu zoonadi zopezeka mu Baibulo. Kutu mudziwe zambiri werengani pa intaneti popita pa www.thegospeltruth.org ndipo muvumere pa email imene mulandire ngati mukufuna kuti mudzilandira nawo kalatayi. Kalata ya *Gospel Truth* imasindikizidwa mu maiko ambiri kuti iperekedwe kwaulere m'dzikomo ndipo chuma chothandizira ntchitoyi chimachokera ku ndalama zimene ena amapereka mwaufulu. Ngati mukufuna lisiti yoonetsa zimene mwapereka, tidzakupatsani. —Editor, Michael Smith

Gospel Truth, P.O. Box 2042, Nixa, MO 65714 USA
editor@thegospeltruth.org

Mau a Mkonzi



Udzwitsitse zoweta zako zili bwanji, samalira magulu ako. —Miyambo 27:23

Mutu wa nkhanu yathu ulendo uno ndiwo wokhudza mfundo za M'baibulo za kasamalidwe kabwino ka chuma. Ndimadzidzimuka chifukwa cha kuchuluka kwa mavesi opezeka m'Baibulo amene akunena za mutuwu. Chinali chondivuta kuti ndichepetse zinthu zochuluka chotere kuti zikwanire mu kalata unoyo amene ali wochepeka kale. Nkhani ya Kukhala Mdindo siikonda kukambidwa pakati pa

anthu a Mulungu ndipo chifukwa cha ichi mabanja ambiri komanso ntchito yolalikira uthenga wabwino zasokonekera chifukwa cha kusasalira ndiponso kukhala mdindo molakwika.

Phunziro la ndalama limakhudza anthu onse ndipo m'mene timasalirira izo zimene Mulungu watipatsa zimakhudzanso kwambiri moyo wathu, kaganizidwe kathu, komanso uzimu wathu, pamene tikuyenda ndi Mulungu. Akhristu ambiri ali akapolo a ndalama mu njira ya ngongole kapena moyo wokonda zinthu. Ambuye atithandize kuti tizigwiritse ntchito ndi kuziyika ndalama pa malo ake oyenerera.


Sizochita kunenanso mochita kukokomezeka tikamakamba za kufunikira kwa ndalama. Mulungu adalitse nkhanu ndipo aike mwa oweranganu njala yofuna kufufuza ndi kudziwa zambiri zimene zalembedwa mu kalatayi. Anthu amatha kudziwa zinthu koma ndi chinthu chapadera ndicho kugwiritsa ntchito mfundo izi zokhudza kasamalidwe kabwino ka chuma. Pezani nthawi ndipo mulingalire za m'mene chilili chuma chanu. Ngati pali pena pofuna kukonza kapena zinthu zina zakuti musamazichite pofuna kuti mulongosole nkhanu yokhudza chuma chanu, teroni ndithu kuti mwakutero mukhoza kukhala mdalitso waukulu kwa anthu ena panopa ngakhale mtsogolomo.

Michael W. Smith

January 2019

MPHAMVU IMENE IPEZEKA POKUNDIKA CHUMA MOSALEKEZA

Sipadzapezeka nthawi yabwino yosunga kapena kukundika ndalama. Anthu ambiri, olemera ndi osauka omwe, amakhulupirira kuti iwo sangakwanitse kukundika ndalama. Zoona zake nzakuti nzotheke kwambiri kuti asunge kapena kukundika ndalama. Kuyambira kwa mlimi wa kumudzi kukafika kwa bwana wogwira ntchito mu ofesi, inoyo ndiye nthawi yokundika ndalama, ngakhale ndalama imene ikusungidwa kuti idzagwire ntchito patsogoloyo itakhala yochepeka. Anthu ambiri akhoza kukwanitsa ndithu kuti asagule chinachake ndi cholinga chakuti akundike ndalama imene akadagulirayo -kaya ndi yokwana mtengo wa fanta kapena tchipisi cha pa chiwaya. Ako kamene kakuoneka kakang'ono kamasanduka chinthu chachikulu pakukundika pang'onopang'ono mosalekeza. Tikasunga ndalama mosadumphitsadumphitsa, nkupita kwa nthawi, ndalamayo imachuluka, choncho yambani kusunga mukadali wachichepere.



M'munsimu muli kuchuluka kwa ndalama zimene tingapeze titamakundika mwezi ndi mwezi kwa zaka zokwanira 40 nkumalandira chionlongozanja cha 8%.

Titachulutsa kapena kuchepetsa nthawi kapena chiongoladzanja, zimenezi zikhonzano kuchulutsa kapena kuchepetsa ndalama zolandira pamapeto. Onani mphamvu imene imapezeka pokundika ndalama pang'onopang'ono mosadumphitsa.

Kukunduka \$5 pamwezi pa chiongoladzanja cha 8% kwa zaka 40 kutipatsa ndalama zokwana \$16,537 [Ndalama zopereka ndi: \$2,400]

Kukunduka \$50 pamwezi pa chiongoladzanja cha 8% kwa zaka 40 kutipatsa ndalama zokwana \$165,373 [Ndalama zopereka ndi: \$3,600]

Kukunduka \$100 pamwezi pa chiongoladzanja cha 8% kwa zaka 40 kutipatsa ndalama zokwana \$330,747 [Ndalama zopereka ndi: \$48,000]

Kukunduka \$1,000 pamwezi pa chiongoladzanja cha 8% kwa zaka 40 kutipatsa ndalama zokwana \$3,307,470 [Ndalama zopereka ndi: \$480,000]



Mukafuna kutipeza

pa intaneti, mulembe

www.thegospeltruth.org

kuti mudzilandira makalata

athu kapenanso kuti

muone makalata akale.

Kalozera posanthula Mau a Mulungu

Mutu: Kukhala mdindo pachuma

Kuwerenga Malemba: Komatu pano pafunika za adindo, kuti munthu akhale wokhulupirika. —1 Akorinto 4:2

Mwachidule: Ziphunzitso komanso mfundo za udindo wathu pa chuma ndi gawo lofunikira kwambiri mu Chipangano Chakale ndi Chatsopano. Mwana wa Mulungu akuyenera kuyang'anira zinthu zadziko mokhulupirika ndi moona mtima. Kupanga dongosolo lakayendetsedwe ka chuma potsatira zimene malemba akunena ndi chinthu chofunikira ndipo zimathandizira kuti Mkhristuyo agwire ntchito, alipire zinthu, apereke komanso akonzekere za tsogolo lake molingana ndi kupereka ndiponso chisamaliro cha Mulungu.

Tanthauzo: Kukhala mdindo —Kuyang'anira ndi kusamalira bwino kwa chinthu chimene atipatsa kuti tichisamalire.



I. Kukhala mdindo

- A. Yakobo 1:17 Mphatso iliyonse imachokera kumwamba.
- B. 1 Akorinto 3:9 Antchito pamodzi ndi Mulungu (1 Akorinto 4:2).
- C. Luka 16:10-11 Kukhala wokhulupirika ndi ndalama.
- D. Mateyu 25:14-30 Fanizo za matalente.

II. Kagwiridwe ntchito kabwino

- A. Aroma 12:11 Osachita ulesi pa malonda (Miyambo 10:4).
- B. Miyambo 24:30-34 Munda wa waulesi.
- C. 2 Atesalonika 3:10-13 Mugwire ntchito kuti mudzipereke chakudya.

III. Perekani

- A. Machitidwe 20:35 Kupatsa kutidalitsa koposa.
- B. 2 Akorinto 9:6-7 Wopereka mokondwera.
- C. Duteronomo 16:17 Perekani m'mene mungathere.

IV. Patsani banja lanu zosoweka zake

- 1 Timoteo 5:8 Samalirani banja lanu ndi kulipatsa zosoweka zake.

V. Kukhala oona mtima ndi wolungama

- A. Miyambo 22:1 Mbiri yabwino.
- B. Miyambo 22:16 Musazunze aumphawi.
- C. Duteronomo 25:13-15 Muyezo wolungama.

VI. Lipirani zofunikira komanso antchito

- A. Levitiko 19:13 Perekani malipiro panthawi yake (Yeremiya 22:13).
- B. Yakobo 5:4 Musachite chinyengo.

VII. Lipirani Msonkho

- A. Mateyu 22:17-21 Perekani kwa Kaisara.
- B. Aroma 13:7 Perekani kwa amangawa komanso a msonkho.

VIII. Ngongole

- A. Miyambo 22:7 Okongola amakhala kapolo kwa wokongoza.
- B. Aroma 13:8 Musakhale ndi ngongole ndi munthu aliyense.
- C. Masalmo 37:21 Anthu oyipa sabweza ngongole.
- D. Miyambo 22:26-27 Musakhale chikole pa ngongole ya wina.

IX. Pangani dongosolo komanso pangani bajeti

- A. Luka 14:28-30 Werengetserani bwino lomwe.
- B. Miyambo 27:23 Dziwani m'mene ziliri zoweta zanu.

X. Sungani ndipo kundikani

- A. Miyambo 6:6-8 Pitani kwa nyererere.
- B. Miyambo 21:20 Anzeru amasunga chuma chawo.
- C. Genesis 41:34-36 Yosefe mu Eguputo
- D. Mateyu 13:44-46 Kugula ndi kugulitsa (Miyambo 31:16).
- E. Miyambo 13:22 Musiye cholowa.

XI. Machenjezo

- A. Mlaliki 5:10 Chuma sichikhutitsa.
- B. 1 Timoteo 6:17-18 Musakhulupirire chuma.
- C. 1 Timoteo 6:9-10 Chikondi cha pa ndalama.
- D. Luka 12:15 Chenjerani ndi kusirira.
- E. Mateyu 13:22 Chuma chimanyenga.
- F. 1 Yohane 2:15-17 Musalikonde dziko lapansi.
- G. Marko 8:36 Kodi zipindula chiyani?

XII. Khulupirirani mwa Mulungu

- A. Mateyu 6:19-33 Tumikirani Mulungu osati ndalama, popeza Atate wanu amadziwa zomwe mumazisowa.
- B. Afilipi 4:11-13 Mukhale wokwaniritsidwa (Ahebri 13:5-6).
- C. Afilipi 4:19 Mulungu adzakupatsani.
- D. 1 Petro 5:7 Mulungu amakusamalirani.

Kumaliza

Chifukwa chake ngati simunakhala okhulupirika m'chuma cha chosalungama, adzakhulupirira inu ndani ndi chuma choona? — Luka 16:11

MFUNDO ZA BAIBULO ZOKHUDZA KUKHALA MDINDO PACHUMA

Malemba amatsindika njira zambiri zodziwika bwino zokhudza kukhala mdindo pachuma zimene tikazitsatira zikhoza kutibweretsera mtendere wa mumtima komanso kukhazikika.

Kugwira bwino ntchito

Akhristu akuyenera kukhala anthu otakataka ndi olimbikira pogwira ntchito, osati aulesi pa zinthu zadziko (Aroma 12:11). Pa Miyambo 24:30-34 akulongosola za munda wa munthu waulesi amene salabadira za munda wakewo. Chifukwa chosamamala ndi kusayikapo mtima, mundawo sunabereke zokolola zoyenera ndipo umphawi unafika. Adindo a chikhristu akuyenera kukhala ogwira bwino ntchito komanso olimbikira kugwira ntchito, osunga nthawi, komanso kuchita zinthu mwapamwamba. Mtima wongofuna



“Adindo a chikhristu akuyenera kukhala ogwira bwino ntchito komanso olimbikira kugwira ntchito, osunga nthawi, komanso kuchita zinthu mwapamwamba.”

kulandira ndi wosiyana ndi malemba. Pa 2 Atesalonika 3:10-12 akunena kuti, “Ngati munthu safuna kugwira ntchito, asadyenso.” Paulo anawalamula anthuwo amene samagwira ntchito chifukwa cha ulesi kuti “adye chakudya cha iwo okha.” Kuyambira pamene Adamu anagwa, munthu anapatsidwa ntchito yakuti adzigwira komanso kuti adzidya chakudya chimene wachikhetsera thukuta ndiponso chimene wachigwirira ndi manja ake.

Perekani kwa Mulungu poyamba

Pamene zokolola zacha ndipo dzakumunda dzakololedwa, ndipo antchito alipidwa kapena ndalama tazipeza kuchokera mu njira zina, kumbukirani kuti ndi Ambuye. Mdindo wabwino sagwiriziza ndalama za Ambuye koma amazigwiritsa ntchito monga m'mene anamulangizira Ambuye. Ndi cholinga cha Mulungu kuti adindo ake apereke mwaulere ndi mosatonzera pofuna kuthandiza pa ntchito ya uthenga wabwino komanso osauka. “Aperereke yense monga mwa mphatso ya m'dzanja lake, monga mwa mdalitso wa Yehova Mulungu wanu anakupatsani” (Duteronomo 16:17). Ngakhale kuti kupereka chakhumi ndi chiphunzitsa cha mu Chipangano Chakale, kupereka kuli gawo lofunikira la kukhala mdindo. Adindo akuyenera kupereka mokondwerera ndi mosachita kukakamizidwa (2 Akorinto 9:6-7), popeza Ambuye anati, “Kupatsa kutidalitsa koposa kulandira” (Machitidwe 20:35). Tipereke poyamba zimene tazipeza poyambirira pa zokolola kapena ndalama zathu ndipo tipereke mosadumphitsa ndi mokhulupirika, ngakhale kuti pali zinthu zina zimene zikufuna ndalama.

Patsani zosoweka za pa banja lanu

Pa 1 Timoteo 5:8 akutipatsa dongosolo lenileni la udindo wa bambo m'banja. “Koma ngati wina sadzisungiratu mbumba yake ya iye yekha, makamaka iwo a m'banja lake, wakana chikhulupiriro iye, ndipo aipa koposa wosakhulupirira.” Ngakhale kuti poyamba tidziganizira za Mulungu pa kugwiritsa ntchito kwa ndalama zathu, bambo akuyenera kugwiritsa ntchito ndalama zake pofuna kukwaniritsa zosoweka za mkazi ndi ana ake. Munthu amene akudzinena kuti ndi mkhristu koma namagwiritsa ndalama zake pa zinthu zina koma osasamalira banja lake ameneyo ndi oipa kuposa wina amene amamukana Mulungu.

Khalani oona mtima ndi olungama

Pali njira zambiri zopezera ndalama, koma mdindo wabwino achite zonse zothekera mwa umunthu wake komanso kuyendetsa bizinesi yake mokhulupirika ndi mwachilungamo. “Mbiri yabwino ifunika kopambana chuma chambiri” (Miyambo 22:1b). Pali anthu m'dziko lino amene amapanga ndalama kudzera m'njira zachinyengo kapena kuwadyera anthu ena masuku pamutu. Koma Baibulo silivomereza zimenezo. “Wotsendereza waumphawi kuti achulukitse chuma chake... angosauka.” (Miyambo 22:16). Pa Duteronomo 25:13-15 amatiphunzitsa kuti muyezo umene tigwiritsa ntchito udzikhala woona ndi wachilungamo. Mwa njira ina, padzikhala kuchita mokhulupirika pa bizinesi ya mtundu wina uliwonse ndipo tisagwiritse ntchito njira zachinyengo ndi cholinga chofuna kuwabera anthu. Machitidwe a chinyengo pa bizinesi ndi zina mwa zinthu zimene zikhoza kupangitsa kuti mkhristu adzionengere mbiri yake yabwino kapenanso kuononga mbiri ya anthu a Mulungu mu dera limene iye akukhala.

Lipirani mabilu komanso antchito anu

Nkofunikira ndi koyenera ndithu kuti mdindo wokhulupirika achite zonse zotheka kuti alipire ogwira ntchito komanso mabilu onse kwathunthu komanso panthawi yake. Yereimiya 22:13 ndi Levitiko 19:13 akuchenjeza za kumuchenjerera mnzako posamulipira atakugwirira ntchito imene unamuuzza kuti agwire. Ngati tamuuzza munthu kuti agwire ganyu koma osamulipira kapena tagwiritsa ntchito madzi kapena magetsi koma osalipira, kumeneko ndi kuba ndithu. “Taonani, mphotho ya antchitowo anasenga m'minda yanu, yosungidwa ndi inu powanyenga, ifuula; ndipo mafuulo a osengawo adalowa m'makutu a Ambuye wa makamu.” (Yakobo 5:4). Kukhala kwa chikhristu komanso kukhala oona mtima kumatifulumiza kuti titsatire mfundo iyi ya kukhala mdindo wabwino wa chuma.

(Yapitirira pa tsamba 6)

Kupereka ngongole

Tchimo lalikulu m'maiko mwina ndiko kuchita chinyengo polipira ndalama za msonkho zimene timapereka ku boma. Komatu Baibulo limakamba izi momveka bwino ndipo si nkhani yakuti mdindo wachikhristu adzikhala akufunsa ngati zili zoyenera kapena ayi. Yesu anati, "Chifukwa chake patsani kwa Kaisara zake za Kaisara" (Mateyu 22:21). Iye amanena za kufunikira kopereka msonkho ku boma limene lisali lachikhristu. Pa Aroma



13:7 akupitirira kuthira ndemanga pa nkhanayi pamene akulangiza oyera mtima kuti alipire "kwa anthu onse mangawa ao; msonkho kwa eni ake a msonkho." Akhristu akuyenera kulipira icho chimene boma limalamulira molingana ndi lamulo loyikidwa ndi bomalo

Ngongole

Pa Aroma 13:8 akunena kuti, "Musakhale ndi mangawa kwa munthu aliyense, koma kukondana ndiko." Baibulo silikaniza kubwereka ngongole koma limaphunzitsa kuti ngongole zonse za ndalama zibwezedwe kwa eni ake. Ngongole ya chikondi ndi yokhayo imene imene sitingakwanitse kuyibweza kwathunthu. Malemba ochuluka amanena za ngongole koma sakaniza kubwereka ndalama komanso kutenga ngongole. Malemba amatichenjeza momveka bwino za kuopsa kobwereka ndalama. Ngongole ikhoza kumudya wokongolayo ndipo ikhoza kusokoneza chimwemwe ndi mtendere za mwana wa

Mulungu. Chifukwa cha chimenechi, ngongole ndi ndalama zimakhala zinthu zauzimu. Pa Miyambo 22:7 akunena kuti, "ndipo wokongola ndiye kapolo wa womkongoletsa." Anthu ambiri ali akapolo a ngongole ndipo ali m'mavuto aakulu a ndalama. Cholinga cha Mulungu pa ana ake ndicho chakuti iwo amasulidwe ku ukapolo woterewu. Kukhala mfulu ku ngongole kumabwera popanga chisankho chakuchita zonse zothekera komanso kudzipereke kuti ubweze ngongole ndi kukhala womasuka ku goli lake. Ngati mkhristu akongola ndalama, iye akuyenera kubweza ngongoleyo kaya itenga nthawi yotalika motani. Anthu oipa mtima ndi amene amatenga ngongole koma osabweza ngongoleyo (Masalmo 37:21).

Ngongole ndi msampha wa mdani ndipo miyoyo yambiri yataika chifukwa cha zisankho zolakwika zokhudza chuma. Nthawi zambiri ngongole imabwera chifukwa chakuti tagwiritsa ntchito ndalama koposa zimene tili nazo makamaka pogulira zinthu zodula kwambiri kapenanso zosafunikira. Kudzikuza, umbombo ndi dyera lofuna kugula zinthu zambiri makamaka mu m'badwo uno zationonga ndipo tikuyenera kusamalitsa pogwiritsa

ntchito khadi ya ku banki pofuna kulipira zinthu. Mabanja ambiri achichepere amasiku ano amafuna kukhala ndi zinthu lero zimene makolo awo ali nazo koma ngakhale angogwira ntchito kwa zaka zochepa. Chifukwa cha chimenechi, iwowo amagwa mu ngongole. Umenewu ndi msampha wa mdaniyo ndipo anthu ambiri makamaka achinyamata akuyenera kusamala nalo khwekhwe limeneli pa nkhani za ndalama. Pamene anthu ali mu ngongole, chimwemwe chawo chimasokonekera, komanso sakhala ndi chuma chokwanira kuti akhoza kupereka ku ntchito ya Mulungu monga m'mene akanafunira. Mulungu akufuna kuti kagwiritsidwe ntchito ka ndalama zathu kakhale kodzisunga ndiponso moyo wathu tikhale ndi zinthu zochepa komanso zosalowa m'thumba kwambiri ngakhale titakhala kuti tikhoza kukwanitsa kukhala ndi zinthu zamtengo wodula zimene tingazipeze m'moyo uno.

Pangani dongosolo komanso pangani bajeti

Yesu analankhula za kufunikira kwa kuwerengera chuma chimene chidzafunike pa nyumba imene munthu akumanga asanayambe kuyimanga kuti adziwe ngati ali ndi ndalama zokwanira zomalizira nyumbayo (Luka 14:28-30). Apa pali phunziro la tsiku ndi tsiku komanso lofunikira kwambiri lokhudza kukhala mdindo pa chuma. Ndi chinthu chanzeru kukhala ndi dongosolo lachuma komanso bajeti ya m'mene mugwiritsire ntchito ndalama pa kugula zinthu, kupereka ndiponso kusunga, zonsezi molingana ndi m'mene ziliri ndalama zanu. Nkofunikira kulemba mndandanda wa zimene mukuyembekeza kuti zilowa komanso zimene mugwiritse ntchito ndipo ndalamazo zikabwera nkutsatira zimenezo. Anthu ambiri sasamalira bwino chuma chawo ndipo sadziwa kuti chuma chawo chikuyenda bwanji. "Udziwitsitse zoweta zako zili bwanji, samalira magulu ako" (Miyambo 27:23). Kukhala ndi chidziwitso kumatithandiza kuti tipange zisankho zabwino. Kupanga dongosolo lachuma komanso bajeti ndi chinthu chofunikira kwa olemera ndi osauka omwe.

Sungani komanso kundikani

Kusunga komanso kukundika ndalama nthawi zina kumaoneka ngati kusowa chikhulupiro, komatu Mau a Mulungu amanena momveka bwino za kufunikira kwa kusunga kuopera pa mawa. "Pita kunyerere, waulesi iwe, penya njira zao nuchenjere; ... koma zitengeratu zakudya zao m'malimwe; nizituta dzinthu zao m'masika" (Miyambo 6:6-8). Langizo la Mulungu kwa Farao ku Eguputo kuja linali lakuti asunge m'nthawi ya dzinthu dzochuluka pofuna kukonzekera nthawi ya chilala (Genesis 41:34-36). Munthu wanzeru amasunga ndi kukundika podziwa kuti idzafika nthawi pamene adzakalamba ndipo sangathenso kugwira ntchito ndipo mapezedwe a ndalama adzakhala ochepa. Zaka zina zokolola zimakhala zochuluka pamene mu zaka zina zimakhala zochepa, nchifukwa chake kumafunika kukonzekera ndi kupanga dongosolo labwino la m'mene ziwirizi zingathandizirane.

Yesu ananena fanizo la munthu amene anagulitsa zonse zimene anali nazo ndi cholinga chakuti agule chuma cha mtengo wapatali chimene chinali m'munda wina. Yesu amagwiritsa ntchito mfundo ya chuma ya kukundika pofuna kulongosola za mfundo yauzimu (Mateyu 13:44-46). Iye anagwiritsanso ntchito mfundo yofanana nayo mu fanizo la matalente ponena za munthu wina amene

anabisa talente lake pansi ndipo sanalipindulitse kwa okongozo ndalama kuti alilandire ndi chiongoladzanya. Ndi chinthu chanzeru kusunga ndalama komanso mkukunduka pang'onopang'ono kwakanthawi kuti ikhoza kudzagwira ntchito mu zaka zimene chuma chidzakhala chochepe. Nthawi yabwino yosunga komanso kukundika ndalama ndi pamene munthu ukadali wachinyamata. Nthawi zambiri padzakhala njira zambiri zakuti mukhoza kugwiritsira ntchito ndalama, komatu ndi munthu wanzeru yekha amene amaika padera nasunga mosaphonyetsa ndalama yakuti adzagwiritse mtsogolo.

Machenjezo

Ngakhale kuti ndalama ndi yoyenera ndipo ikufunika kuti izigwiritsidwa ntchito mu njira ya umulungu, Baibulo limatipatsa machenjezo ambiri okhudzana ndi m'mene tingachitire ndi ndalama. Chuma sichikwana (Mlaliki 5:10) ndipo Mkhristu sakuyenera kuchikhulupirira poopa “kuti asadzikuze, kapena asayembekezere chuma chosadziwika kukhala kwake, koma mwa Mulungu” (1 Timoteo 6:17-18). Ngakhale kuti Akhristu akuyenera kukhala adindo abwino a chuma, mitima yawo ndi chikondi chawo zisamakhale pa chuma cha moyo uno kapenanso zinthu za dziko lapansi (1 Yohane 2:15-17). “Yang'anirani, mudzisungire kupewa msiriro uliwonse” (Luka 12:15) ndipo chuma chikhoza kukhala chongonyenga ndipo chimatsamwitsa Mau a Mulungu (Mateyu 13:22). Chuma chenicheni chipezeka mwa KhristuYesu ndipo cholinga chathu chachikulu komanso zokhumba zathu zikhazikike pa Iye. “Pakuti munthu apindulanji akadzilemezera dziko lonse, natayapo moyo wake?” (Marko 8:36).

Banja ndi ndalama

Kafukufuku waonetsa kuti ndalama ndi chimodzi mwa zifukwa zimene zikuyambitsa mavuto m'mabanja komanso chimene chikupangitsa kuti maukwati adzitha. Nkhani zokhudza ndalama zikhoza kudzetsa mpungwepungwe m'banja komabe izi zikhoza kuchepetsedwa ngati titatsatira mfundo izi zochokera m'baibulo.

Pamene amalankhula za banja pa Mateyu 19:6, Yesu ananena kuti mwamuna ndi mkazi sanalinsu anthu awiri koma ndi thupi limodzi. Mfundoyi imakhudza koposera pa kulumikizana kwa awiriwo ngati thupi. Banja kwenikweni ndiwo umodzi komanso kulunzantsidwa pamodzi ndipo zimenezi zimakhudza ngakhale magawo a chuma. Pamene tikulemekeza kuti pamakhala machitidwe osiyanasiyana pakati pa miyambo, tikuyenera kudziwa kuti mabanja amakhala olimba ngati nkhanu zokhudza chuma tizipangira limodzi. Chinthu china chimene chimachitika ndicho chakuti timayika chotchinga ngati mmodzi mwa awiriwo akhala ndi umwini komanso ntchito yosamalira ndalama kusiyana ndikuti onse awiriwo agwiritsire limodzi chuma chawo pa kugulira zinthu, kusunga ndi kukundika ndalama limodzi. Moyo wakuti mmodzi mwa iwo adzingogawiridwako ndalamazo ukhoza kupangitsa kuti winayo zidzimupweteka.



Khulupirani mwa Mulungu

Akhristu akuyenera kuyika chikhulupiriro chawo mwa Mulungu wamoyo, osati mu zinthu za dziko lino. Atate wathu wakumwamba amadziwa zimene ifeyo timafuna ndipo adzasamalira ana ake (Mateyu 6:19-33). Ngakhale kuti izi sizisutsana ndi mfundo zabwino za chuma, mtima ndi maganizo a mkhristu pa nkhanu ya ndalama ndi zosiyana ndi za anthu a dziko lapansi. Mkhristu akuyenera kuzindikira ntchito ndi udindo wa chuma komanso katundu kwinauku nkukhala ndi mtima wodalira ndiponso kukhulupirira mwa Mulungu mwini. Mwana wa Mulungu akuyenera kuphunzira kukhala wokhutitsidwa (Afilipi 4:11-13) ndipo akhale modekha podziwa kuti “Koma Mulungu wanga adzakwaniritsa chosowa chanu chilichonse monga mwa chuma chake m'ulemerero mwa Khristu Yesu.” (Afilipi 4:19).

Ambuye adalitse mwana aliyense wa Mulungu kuti ayikepo mtima ndi kuphunzira maphunzitsa ndi nzeru zopezeka mu mfunso izi zochokera m'baibulo zokhudza kukhala mdindo wabwino wa chuma. Anthu ena, pofuna za dziko komanso ena pofuna chilungamo sanazilabadire mfundozi ndipo zotsatira zake ndi zakuti asautsika ku uzimu ndi kugawo la zachuma lomwe. Ngakhale kuti umphawi kapenanso kulemera si zizindikiro za uzimu, kukhala mdindo kwa munthu ndi chinthu chimene chimaonetsera kuti iye amamvera Mau a Mulungu. Pali mdalitso umene ukudikira iwo amene atsatira ndi mtima wao wonse zimene Malemba akunena pa nkhanu. Ngati tikhala osakhulupirika ndi ndalama komanso zinthu za dziko lino, kodi nanga Mulungu angatikhulupirire bwanji ndi chuma chenicheni cha ufumu wa Mulungu? (Luka 16:11). ■

Zimakhala bwino kwambiri kuti masankho a m'mene mungachitire ndi ndalama zanu muchitire limodzi. Kulumizana ndiyo njira imodzi yothandiza pofuna kuchepetsa mavuto amene amabwera m'banja chifukwa cha ndalama. Kugwirizana zochita pa zokhudza ndalama m'banja ndi chinthu chofunikira kwambiri pofuna kuti zinthu ziyende bwino m'banjalo. Kugwirizana limodzi bajeti yanu komanso zimene muchite ndi ndalama zanu zikhoza kuthandiza kuchepetsa kukangana ndi kukayikirana kumene kumabwera tsiku ndi tsiku pa nkhanu zokhudza m'mene mukuonongera ndalama zanu m'banjamo. Pamene tikambirana mfundo zimene titsatire poyendetsa chuma cha m'banja mwathu, zikhoza kuoneka ngati mwina munthu mmodzi akufuna kumalamulira, chifukwa cha ichi nfofunika kukambirana mwa chisomo, mwaulemu komanso molemekeza mfundo ya mzanuyo. Mwamuna ndi mkazi wake aonetse kuti akulemekeza kusiyana kwa udindo ndi ntchito zimene aliyense wa iwo angakwaniritse panyumbapo, komabe kwinauku akugwirira ntchito limodzi pofuna kuti chuma chawo chiyende bwino komanso akhale ndi mtendere wa mumtima. ■



KODI MUKUDZIWA?

Ngongole yabwino ndi ngongole yoipa

Ngongole zonse sizili zofanana. Ngongole yabwino imatanthauza ngongole imene imatithandiza kuti tipeze chuma kapena imene kumapeto ake timatukuka nayo monga maphunziro, kupangira bizinesi, kumangira nyumba, kapenanso kukundika kuti ndalama zidzachuluke. Ngakhale zili choncho, si nthawi zonse pamene titatenga ngongole ngati iyi pomwe zidzatiyendere, popeza nthawi zina zinthu zimatha kusokonekera.

Ngongole yoipa ndi imene timatenga kuti tigule zinthu zimene pamapeto ake zimasuluka mphamvu ngati magalimoto, zovala, katundu wam'nyumba ndi zinthu zina. Amene amagula zinthu pangongole pogwiritsa ntchito khadi ya ku banki (makamaka m'maiko akunja ndi olemera) amakhala pa ngongole yaikulu popeza chindapusa chake chimakhala chachikulu ngati sayibweza m'nthawi yake. ■



Mau a pa
Nyengo
Yake

MULUNGU AKUDZIWA KUTI MUMAZIFUNA ZINTHU ZONSEZI

Chifukwa chake musadere nkhawa, ndi kuti, Tidzadya chiyani? ... Kapena, Tidzavala chiyani? ... Pakuti Atate wanu wa Kumwamba adziwa kuti musowa zonse zimenezo. Koma muyambe mwafuna Ufumu wake ndi chilungamo chake, ndipo zonse zimenezo zidzaonjezedwa kwa inu. —Mateyu 6:31-33

Nthawi zambiri, atumiki amene ali odzipereka ndi odzikhuthula pa ntchito ya uthenga wabwino amakumana ndi mavuto a zachuma komanso umphawi pamene akukangalika kugwira ntchito molimbika pofuna kutukula chuma cha Khristu kusiyana ndi kutumikira mulungu wa chuma wa dziko lino. Pamene tikuyenera kugwiritsa ntchito nthawi ndiponso matalente athu pofuna kupititsa patsogolo ufumu wa Mulungu, ndalama ndi chinthu chofunikira kwambiri pamene tikukhala m'dzikoli. Mulungu akudziwa bwino za chimenechi ndipo sangawayiwale atumiki ake m'nthawi yawo ya kusowa. Atumiki a uthenga wabwino akuyenera kukhala wokonzeka kuti azunzike pamene akuima njii pa chikhulupiriro chawo popeza Mulungu walonjeza kuwapatsa zofunikira zawo. Mu nthawi zovuta, chikhulupiriro chathu chidzikwera kuposera pa zofuna zathu makamaka pozindikira kuti Mulungu ali ndi cholinga komanso chifuniro chachikulu.



Kuti Mutipeze

The Gospel Truth
P. O. Box 2042
Nixa, MO 65714
USA

Email:
editor@thegospeltruth.org

CHIYERO CHA KWA AMBUYE

Mau a Paulo pa Afilipi 4:11-13 atitsutse tonsefe: “Si kuti ndinena monga mwa chiperewero, pakuti ndaphunzira ine, kuti zindikwanire zilizonse ndili nazo. Ndadziwa ngakhale kupeputsidwa, ndadziwanso kusefukira; konseko ndi m'zinthu zonse ndalowa mwambo wakukhuta, ndiponso wakumva njala; wakusefukira, ndiponso wakusowa. Ndikhoza zonse mwa Iye wondipatsa mphamvuyo.” Mulungu watsimikizira za chikondi ndi chisamaliro chake ndipo sadzakusiyani ngati mukhala okhulupirika kwa Iye komanso kukhala m'moyo wakuti Iyeyo alandire ulemerero.

Chikhulupiriro sichitsutsa mfundo zina za kukhala mdindo. Ngakhale kuti tili ndi chuma chotani, nkofunikirabe kuti utumiki wathu ugwiritse mfundo zabwino zoyendetsera chuma chathu pokhala adindo abwino. Atumiki adzisunga ndalama kuchitira pamawa monga m'mene amachitira wina aliyense, komabe asakhulupirire chumacho, popeza chili ngati mchira wa khoswe umene suchedwa kupululuka. Musanyengeke nkumaganiza kuti mukhoza kusakaza lero nkumayembekezera kuti Mulungu adzasamalira za mawa lanu. Zikhoza kukhalatu kuti Mulungu akukudalitsani lero ndi cholinga chakuti musunge ndalama ndi kukhala ndi chakuti mukhoza kudya mwezi wamawa.

Mulungu, pokhala atate wathu wakumwamba, amadziwa mavuto amene mumakumana nawo ndiponso nkhawa zokhudza chuma zimene mumakhala nazo pa tsogolo la banja lanu. Muike maso anu pa Khristu ndipo musachepetse utumiki umene muli nawo wolalikira uthenga wabwino potsata zinthu zakutha za dziko lino. Mulungu adzakhala okhulupirika pa Mau ake ndipo adzakutumikirani molingana ndi chosowa chanu. ■